# CHIMUTU CLUSTER EXAMINATION BOARD

**2024 END OF TERM TWO STANDARIZED EXAMINATION FOR STANDARD 6**

**CHICHEWA**

**(100 MALIKISI)**

**Tsiku: _____ / ____/ 2024** **Nthawi: ______________**

**DZINA LA OPHUNZIRA: ____________________________________________________________________**
(Surname first)
**DZINA LA SUKULU: ________________________________________________________________________**

**MALANGIZO**

- Onetsetsani kuti pepala lanu lili ndi magawo anayi A, B, C ndi D
- Lembani chimangirizo kapena kalata mugawo A ndipo muyankhe mafunso onse m'magawo B, C ndi D
- Yankhani mafunso a mu gawo D pozunguliza limbo lokhoza

**GAWO A (30 MALIKISI)**

**Lembani chimangirizo kapena kalata. Mawu a chimangirizo kapena kalata yanu asachepere 100 komanso asapitilire 150**

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu '**MALONDA**. Mwa zina tsatani izi polemba
   **Ndime yoyamba**
   - Fotokozani malo awiri m'dera lanu komwe malonda amachitikira
   - Tchulani zinthu zomwe zimagulitsidwa pamalowa

   **Ndime yachiwiri**
   - Perekani masiku omwe anthu amachita malonda pamalowo
   - Fotokozani ubwino wa malonda

   **Ndime yachitatu**
   - Fotokozani mavuto omwe anthu ochita malonda amakumana nawo
   - Tchulani njira zomwe ochita malondawo angatsate kuti athane ndi mavutowo

**KAPENA**

2. Lembani kalata kwa nzanu yomufotokozera mbewu zomwe mumalima m'dera lanu. Mwa zina tsatani izi polemba kalata yanu
   **Ndime yoyamba**
   - Cholinga cha kalata yanu
   - Dera lomwe mumakhala
   - Mitundu ya mbewu zomwe zimalimidwa m'deralo

   **Ndime yachiwiri**
   - Nyengo yomwe mbewuzo zimalimidwa
   - Zofunika pa ulimi wa mbewuzo
   - Kasamalidwe ka mbewuzo

   **Ndime yachitatu**
   - Fotokozani phindu lomwe anthu amapeza kuchokera ku mbewuzo

________________________________________________________________________________

________________________________________________________________________________

________________________________________________________________________________

________________________________________________________________________________

## GAWO B (MALIKISI 20)
## KUMVETSA NKHANI

3. Werengani nkhani yotsatirayi ndipo muyankhe mafunso omwe ali kumapeto kwa nkhaniyi

Edzi ndi matenda amene amayamba kaamba kakuchepa kwa chitetezo mnthupi. Tikhoza kunena momasuka kuti edzi ndi chipwirikiti cha matenda osiyanasiyana chifukwa chakuchepa kwa chitetezo mnthupi. Ena mwa matenda omwe amalowa mnthupi chifukwa cha kuchepa kwa chitetezo ndi monga: chifuwa chachikulu (TB) chibayo, khansa ndi kutsegula m'mimba. Zonsezi zimachititsa wodwala edzi kuwonda. Dziwani kuti HIV si matenda koma ndi kachilombo koyambitsa edzi. Tidziwenso kuti anthu amene alibe kachirombo ka HIV amadwalanso matenda tatchulawa.

Pali njira zingapo zomwe anthu angapatsirane kachirombo ka HIV komwe kamayambitsa Edzi. Njira yaikulu yomwe anthu angapatsirane kachiromboka ndikuchita chiwerewere kapena kugonana mosadziteteza ndi munthu yemwe ali ndi kachiromboka. Ena amatha kutenga kachiromboka pobadwa kuchokera kwa makolo awo omwe ali nako. Njira zina ndi monga kulandira magazi kuchokera kwa munthu yemwe ali ndi kachiromboka, kubwerekana malezala, zingano komanso mswachi ndi munthu amene ali ndi kachilomboka.

Tingathe kupewa kachilombo ka HIV pozindikira mafalidwe ake popeza kupewa kuposa kuchiza. Sibwino kupisa chala kudzenje komwe ukudziwa kuti kuli njoka. Maiko ambiri achepetsa kufala kwa kachilomboka popewa njira zomwe kachilomboka kamafalira. Tiyeni ife monga a Malawi tichite chimodzimodzi kuti mtundu wathu upitilire.

Mafunso

(a) Kodi edzi ndi chiyani?

____________________ malikisi 2

(b) Tchulani matenda awiri amene munthu amadwala chifukwa cha Edzi

____________________

____________________ malikisi 2

(c) Fotokozani kusiyana kwa HIV ndi Edzi

____________________

____________________

____________________

____________________ malikisi 4

(d) Tchulani njira zitatu zomwe anthu angapatsirane kachilombo ka HIV

____________________

____________________

____________________ malikisi 3

(e) Perekani njira yaikulu yomwe anthu angapatsirane kachilombo ka HIV

____________________ malikisi 1

(f) Tchulani njira zitatu zopewera kutenga kachilombo ka HIV

____________________

____________________

____________________ malikisi 3

(g) Lembani matenda awiri omwe amafala m'njira yogonana kupatula Edzi

____________________

____________________ malikisi 2

(h) Perekani mawu otsutsana m'matanthauzo ndi awa: kuchokera munkhaniyi

(a) Kunenepa ____________________ malikisi 1

(b) Momangika ____________________ malikisi 1

(i) Perekani mutu wa nkhaniyi

____________________ malikisi 1

## GAWO C (MALIKISI 10)

4. **Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatira**

Chikwana : Odi! Odi!
Nasuluma : Eee! Fikani kakhala pakachikumbapo
Chikwana : Kaya lero mwadzukako bwanji?
Magodi : Aaa! Choncho pang'ono
Nasuluma : Usiku sitinagone achezera kubuula
Chikwana : Tisachedwetu tiyeni tithamangire nawo kuchipatala

**Mafunso**

(a) Kodi ndi malonje anji mwawerengawa

______________________________

(b) Kodi a Magodi ndi ndani m'nkhaniyi

______________________________

(c) Kodi mawu oti kubuula akutanthauzanji m'nkhaniyi

______________________________

(d) Tchulani zinthu ziwiri zoyenera kupezeka pasukulu kuti pakhale paukhondo

______________________________

______________________________

## KUPANGA ZIGANIZO

5. Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa

(a) Mgonero

______________________________

(b) Chiphetsa

______________________________

(c) Wamfupi

______________________________

(d) Gulitsa

______________________________

(e) Pa

______________________________

## GAWO D (MALIKISI 40)

**Zungulizani limbo lokhoza A, B, C kapena D m'mafunso otsatirawa**

**Mafunso 6 mpaka 10: sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo**

6. Mwana **<u>wamwano</u>** sakondedwa
   - A. Dzina C. Muonjezi
   - B. Mfotokozi D. mneni
7. **<u>Iwo</u>** apita ku Dedza
   - A. Mneni C. Mvekero
   - B. Mfotokozi D. Mlowammalo
8. Nabiyeni **<u>waba</u>** chimanga
   - A. Mneni C. Mfuwu
   - B. Muonjezi D. Dzina
9. **<u>Ogo!</u>** Madzi aja atayika
   - A. Dzina C. Mneni
   - B. Mfuwu D. Mlowammalo
10. Aphunzitsi athu amalemba **<u>mofulumira</u>**
    - A. Mfuuliro C. Mlumikizi
    - B. Mfotokozi D. Muonjezi

**Mafunso 11 mpaka 15: perekani matanthauzo a zilapi zotsatirazi**

11. Chiputu zuu! Mbewa lakaa
    - A. Mchenga C. Mtedza
    - B. Chimanga D. Mbatata
12. Ndili ndi ng'ombe zanga zakuda kwambiri
    - A. Madzi C. Mtengo
    - B. Makala D. Nkhuni
13. Alira atadzimenya yekha
    - A. Tambala C. Nkhumba
    - B. Ng'ombe D. Bakha
14. Chimunda chachikulu koma pokolora ndi m'manja
    - A. Chimanga C. Tsitsi
    - B. Soya D. Mtedza

15. Diwa la msenjere kugwaigwa
    A. Mphuno C. Manja
    B. Chikope D. Miyendo

**Mafunso 16 mpaka 20: perekani chachimuna cha mawu awa**

16. Mkwatibwi
    A. Mamuna C. Mkwati
    B. Mkazi D. Mayi
17. Thadzi
    A. Tambala C. Mphunda
    B. Tonde D. Nkhunda
18. Mkota
    A. Chule C. Nyama
    B. Tonde D. Nkhuku
19. Mtsikana
    A. Abambo C. Amayi
    B. Mnyamata D. mwana
20. Chemwali
    A. Mchimwene C. Agogo
    B. Agogo D. Mtsikana

**Mafunso 21 mpaka 25 tsirizani zifanifni zili m'munsizi**

21. Kuda ngati
    A. Makala C. Ngombe
    B. Nkhuku D. Mbuzi
22. Kuwawa ngati
    A. Nsima C. Muwawani
    B. Thobwa D. Mchere
23. Kuchenjera ngati
    A. Fisi C. Kalulu
    B. Nkhosa D. Munthu
24. ________ ngati chitedze
    A. Kukoma C. Kuwawa
    B. Kutsekenera D. Kuyabwa
25. Kutalika ngati __________
    A. Mtengo C. Nyumba
    B. Msungwi D. Munthu

**Mafunso 26 mpaka 30 perekani mitundu ya alowammalo omwe ali ndi mzere kunsi kwawo**

26. **<u>Lanu</u>** lathyoka mpini
    A. Wochuluka
    B. Woloza
    C. Wa dzina lakekale
    D. Waumwini
27. **<u>Ife</u>** tipita kumudzi mawa
    A. Oloza
    B. Wa dzina lakekale
    C. Waumwini
    D. Ofunsa
28. Zalowa **<u>zingati</u>**?
    A. Wa dzina lakelake
    B. Waumwini
    C. Ofunsa
    D. Oloza
29. Uyu akuyang'ana nthochi **<u>izi</u>**
    A. Waumwini
    B. Wa dzina lakelake
    C. Ofunsa
    D. Oloza
30. **<u>Zambiri</u>** zabedwa dzulo
    A. Wochuluka C. Oloza
    B. Oloza D. Wofunsa

**Mafunso 31 mpaka 35 pezani magulu a mayina mziganizo zotsatirazi**

31. Tawina wawedza **<u>mlamba</u>**
    A. I – ZI C. U – MA
    B. MU – MI D. MU – A
32. Ndagula **<u>kadengu</u>** kakang'ono
    A. MU – MI C. U – MA
    B. CHI – ZI D. KA – TI
33. **<u>Khasu</u>** lake lasowa
    A. CHI – ZI C. LI – MA
    B. U – MA D. MU – MI
34. Tiyeni tikamwete **<u>udzu</u>**
    A. LI – MA C. U – MA
    B. I – ZI D. MU – MI
35. Atate agula **<u>chitseko</u>** cholimba
    A. CHI – ZI C. LI – Ma
    B. KA – TI D. U – MA

**Mafunso 36 – 40 tsirizani mikuluwiko yotsatirayi**

36. Ulenje umasimba
    A. Wanga C. Wako
    B. Wamwini D. Wathu
37. Mapanga awiri
    A. Abvumbwitsa C. Anyowetsa
    B. Abwerera D. Ayamikira
38. Ali dere nkulinga utayenda
    A. Nafe C. Nawo
    B. Naye D. Nawe
39. Muvi woyang'anira suchedwa kulowa
    A. Mphuno C. M'manja
    B. Mkamwa D. M'maso
40. Mutu umodzi susenza
    A. Ndowa C. Denga
    B. Dengu D. Thumba

**Mafunso 41 mpaka 45 sankhani chiganizo chomwe chili ndi zizindikiro zamkalembedwe zoyenera**

41. Kodi mukupita kuti
    A. Kodi mukupita kuti.

B. Kodi mukupita kuti?
C. Kodi mukupita kuti!
D. Kodi mukupita kuti,

42. Mmudzi muli uve
    A. M'mudzi muli, uve.
    B. Mmudzi muli uve.
    C. Mmudzi muli uve!
    D. M'mudzi muli uve.
43. Mayo ine wandibaya
    A. Mayo ine wandibaya!
    B. Mayo ine wandibaya?
    C. Mayo ine! Wandibaya.
    D. 'mayo ine wandibaya!'
44. Iye wagula nthochi mtedza chimanga ndi mango
    A. Iye wagula nthochi, mtedza, chimanga ndi mango.
    B. Iye wagula nthochi mtedza chimanga ndi mango.
    C. Iye wagula nthochi, mtedza chimanga ndi mango.
    D. Iye wagula nthochi mtedza chimanga ndi mango?
45. timve wabwera dzulo
    A. timve wabwera dzulo?
    B. timve wabwera dzulo.
    C. Timve wabwera dzulo
    D. Timve wabwera dzulo.

**MAFUNSO ATHERA PANO!!!!!**